



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

NDONDOMEKO YA CHILENGEDWE

Buku la aphunzitsi

Lolembedwa ndi J. N. Sommerville

CHICHEWA VERSION

Cholinga cha bukhu ndi kuyika nsanamira pofananitsa malamulo achikhalidwe ku malamulo athu a kuthupi omwe Mulungu Anaika masiku asanu ndi awiri oyambilira

<http://wisdom-house.cpm/G&V/Spoken Written and Living Word.pdf>

Mu bukhu lotchedwa “Towards Old Testament Ethics”, Dr, Walter C. Kaiser Jr. ananenapo kuti pali mgwirizano pakati pa malamulo achikhalidwe ndi malamulo akuthupi amasiku asanu ndi awiri, otchedwa “Malamulo Polenga”

Malamulo Polenga Dziko

“Nsamamila immodzi yofunikira popanga ziganizo chimachokera mu ntchito ya Mulungu, **Malamulo Polenga**. Awa ndi malamulo amene amaonetsa mmene Mulungu analengera dzikoli ndi zonse zilimo popeza zinalengedwa kuchokera mdzanja la Mulungu. Zimakhudza komanso kuika malamulo pa zonse zamoyo zobereka ana zokhala padziko kuti zili bwino pamaso pa Mulungu, naika udindo olamulira zolengedwa zonse, nakhutitsidwa pantchito yake, napuma tsiku la sabata, ndi kusangalala mmbanja monga mphatso yochoka kumwamba.

Ubwino odziwa mmene dziko linalengedwera ku mabuku a nzeru yakhala ili imodzi mwa zounikira maphunziro a Baibulo. Zomwe zakhala kuti zipangidwe ndi kuti wina apereke ubale pakati pa mmene dziko linalengedwera ndi mfundo zikulu zikulu zachikhalidwe za mma buku a nzeru wa. Komanso, ubale wa malamulo apachiyambi polenga dziko ndi nkhani za mmbanja, umoyo wakugonana, udindo wa makolo, udindo wa adindo ndi owang’anira, katundu, ntchito, moyo, zina zolengedwa zing’onozing’ono ndi zina zotero kukuyenera kukuzidwa tikamaphunzira mtsogolomo. Kuti tikwanitse izi, tikuyenera tiganizire kuti tikhalbe tikudziwitsidwa za kupitiliza kwa mavumbulutso ndikuti zomwe timaganiza poyamba zoti umodzi ndi malamulo a Chipangano Chakale ndizabwino kuposa kuganiza zakusinthana ndi kusagwirizana.

Walter C. Kaiser Jr. “Towards Old Testament Ethics” Tsamba 31

Cholinga cha chomabwereza ma bukuwa ndikuonetsa makhalidwe abwino amene mau a Mulungu. Yesu adati ngati tipitilize mawu ake tidzadziwa chilungamo (Yphane 8:32) ndipo chilungamochi chidzatimasula ife ku nsinga za chikhalidwe cha anthu zomwe zalowelera mumbadwo uno ndipo wabweretsa khungu paliponse.

1 Yohane 1:1 amalumikiza Genesesi, Deutoronome, komanso Yohane Woyera zonsezi pamodzi zikufotokoza zimene Dr. Kaiser akuzitchula kuti “Malamulo apachiyambi”. Ndizithunzi za khalidwe ndi munthu ochokera ku Mawu Olankhulidwa, Liwu Lolembedwa ndinso Liwo La Moyo, Mulengi, Khrikstu.



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

“pakuti kuchokera pachiyambi (“kunayankhuliwa mawu”...kuyere, Gen 1:3) zomwe tinamva (“liwu lolembedwa”... Imvani Israel, Deut 6:4), zomwe tinaona ndi maso athu, zomwe takhala tikuziona ndikuzigwira ndimanja athu (“Mawu a Moyo”... Mawu asanduka thupi, Yohane 1:4), potengera mau a moyo- moyo omwe unaoneker pakati pathu, ndipo tinaona, ndikuuchitira umboni ndipo kuna za moyo osatha, omwe unali ndi Atate ndipo unadzaonekera kwa ife... (1 Yohane 1:1-2)

Yesu anafotokozeredwa mu uthenga wabwino wa Yohane ngati mwachindunji “Mawu a Mulungu”. Anatchulidwanso kuti ndi kuunika kumene kumaoneka mumdiima (Yohane 5:5). Pa mauthenga zana za uthenga wa Yohane, uthenga makumi asanu ndi anayi ndi mpambu ziwiri (92%) umasiyana ndi uthenga omwe mabuku ena atatu a Yohane amanena. Uthenga wa Yohane, umatsutsa kuti Yesu anali mwa umunthu. Yesu ndi kuunika (Yhn 1:4,1Yhn1:5) ndi anthu akudziko ndi mdima (Yhn1:8,1Yhn1:10). Machimo athu amachoka mkati mwathu, osati kwina (Mar7:1-23). Mbuku ili, cholinga chathu ndichosonyeza mawu a Mulungu atafupikitsidwa mu Malamulo khumi ngati malamulo a chikhalidwe ndi chisomo.

Masamba otsatirawa, akutambasula mmene Mawu Asanu ndi awiri komanso zikhalidwe zabwino zisanu ndi ziwiri (zikhalidwe zoyenderana) anakonzedwera kuchoka ku Malamulo khumi. Mawu asanu ndi awiri komanso zikhalidwe zisanu ndi ziwiri ndi zikhalidwe zosiyana ngat momwe kuwala kusiyanalana ndi mdima.

Bukhuli litilimbikitsa kuti tikhale ndi kuzindikira kosiyantsira zabwino ndi zauchimo. “tili ndiizambiri zoyankhura zokhudza izi, ndipo nzovuta kuzifotokoza bwino, chifukwa mwakhala mukuvutika kuzimvetsetsa. Ngakhale pofika pano mukuyenera kukhala muli aphunzitsi, mukufunikabe wina okuphunzitsani nsanamira za masomphenya a Mulungu. Mukufunika mkaka, osati zakudya zolimba, popeza zakudya zolimba ndi za awo okhwima, popeza awo amene ali ndi mphanvu zakusiyantsa zimene munthu umaphunzira poyesa komanso kusiyantsa zabwino ku zauchimo. (Aheb 5:11-14)

Mu buku lawo lotchedwa “Toward Old Testament”, Dr. Walter Kaiser, anationetsa kuti malamulo khumi (Decalogue) atha kugawidwa mmagawo awiri ; Malamulo a ubwino komanso malamulo a kuipa. Mmmalembedwe awo anafotokoza kuti (malamulo awiri oyenderana)”.

...(2) Zilungamo za zikhalidwe zapadziko lonses zikuyenera kumvetsetsedwa mosiyana ngakhalle sizinaikidwe mwa njira yachoncho. Popeza, Mulungu “ankafuna chifundo osati kupereka nsembe” (Hos 6:6, 12:7) komabe kupereka nsembe kunalinso njira imodzi ya vumbulutso. Izi, ndekuti, zikuyenera kumvetsetsedwa mnjira yodziwa choyambilira pone kuti, “tiyambira ichi, kenako tipanga icho” (cf 1sam15:22,sal51:17,19, Yer7:22-23).

(3) Nsanamira za zikhalidwe zoipa ndizo kuvomereza ndipo muzovomereza muli zoipa kuti pamene tchimo lililonse lakanizidwa, udindo osemphana ndikukaniza zoipa umalimbikitsidwa mwa ife ndipo pamene udindowu walimbikitsidwa, tchimo lina lija limakanizidwa. Ndiye, Dute. 6:13 ukutilamula ife kutumikira Mulungu, ndipo tikukanizidwa kutumikira milungu ina-popanda mawu ofotokoza kutiletsa kutero poyera. Chimodzimodzinsu, pamene talamulidwa kulemekeza makolo athu (Eks 20:12), tikukanizidwa kuwatembelera. Kuba ndikoletsedwa (Eks 2015), komano kusamalitsa muntchito zathu komanso ndondomeko zathu zones zinaikidwa.” Walter C. Kaiser Jr. “Towards Testament Ethics” tsamba 65.

KUMASULIRA MALAMULO KHUMI



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

“Kumasulira malamulo khumi a Mulungu sikuti nkovuta ayi, komabe pali zinthu zocheppa chabe zofunika kuzidziwa. Zinthu zake ndi monga

1. Lamulo lathu lachikhalidwe lili ndi mzimu wachikondi kumayambiro mpaka kumapeto kwa lamulo lake. Chinachake chiyenera kuchitidwa chifukwa limatidziwitsa ife khalidwe, chilengedwe komanso mafuno a Mulungu.
2. Malamulo akhumi wa adakanenedwa mwamballi zonse mawubwino komanso molakwikwa , chifukwa pa malamulo achikhalidwe nthawi zonse ali ndi mbali ziwiri. Pamene tikuchita chilichonse mchikhalidwe timakhala tikukaniza mphavu yakutsutsa zochita zathuzo nthawi yomweyo.
3. Mwakudumpha kapena kudzikana kupanga zinthu zoletsedwa sinkhani yachikhalidwe konse ayi, zidakakhala choncho lamulo bwezi likukwanilitsidwa posachita kanthu, zomwe itha kungoti ndi dzina lina la imfa.
4. Pamene choipa chakanizidwa pa malamulo , icho chimatsutsa chabwino chomwe chimafunika kupangidwa wina asanatchulidwe omvera.
5. Kuti ukane chikhalidwe chabwino ndikusankha chinacho, choncho ngati khalidwe labwino silikutsatidwa izi zili ndi mphamvu zokana mphamvu komanso chikhalidwe chabwino.
6. Lamulo silikwanilitsidwa popewa kupanga zinthu zophwanya lamulolo kapena kupanga chinthu china chabwino. Chomwecho sitidzapewa kumuvulaza mzathu kokha iyayi komanso tidzapanga chilichonse ndi mphamvu zathu kuthandiza moyo wa mzathu komanso kuti akhale ndi umoyo wabwino.
7. Lamuloli silitiyankhula ku zochita zathu zokha, komanso ku zotipangitsa, zokopa, kapena zophyinja zotipangitsa kupanga zoletsedwa.
8. Popeza ndiophweka kunena mawu ochepe otsutsana pa malamulowa, ndipo zotsutsa zifuna kukumana ndi funde la zoipa mmitima mwa anthu, malamulo ambiri nawo ndiwotero. Koma ufulu wathu mwa zisomo ndiwaukulu kwambiri kotero nkovuta kupereka malangizo bwino bwino potengera ndi chidule cha mmene malamulowa anaikidwira. Walter C. Kaiser Jr. “Towards Testament Ethics” tsamba 83,84

Cholinga choyambilira ndichoti tionetsere poyera mmene Malamulo khumi atha kugawidwira mzigawo zotstsana kudzera mnjira zinayi zotsatirazi.

1. Lembani Malamulo onse khumi (Eks 20, Deut 5)
2. Lembani mndandanda ogwawidwa mu tebulo, Mkagawo kotsika koyamba, lembanimu malamulo omwe ali otsutsa (monga “Zomwe Mulungu analetsa kuchita”), mkagawo kena kotsika, ikanimo malamulo omwe siotsutsa (monga “zomwe Mulungu anati tizichita”).
3. Muonjezere motsitsa ena malamulo achikhalidwe kumbali zonse, zotsutsa kuziika kumbali ya Malamulo otsutsa, ndizolangiza kumbali ya malamulo olangiza. Mwachitsanzo, tikuyenera kumvera makolo, sitikuyenera kuwagalukira (Aef 6:1-2). Sitikuyenera kuba, tikuyenera kugwira ntchito ndi manja athu (tikhale osamalira), Aef 4:28; sitikuyenera kuwanamiza pakati pathu, mmalo mwake tiuzane chilungamo. Aef 4:25.
4. Lembani liwu limodzi lofupikitsa Malamulo khumi onse, kusiyantsa kwa khalidwe lalembedwa. Chitsanzo, usabe wafupikitsidwa kuti umbava; kugwira ntchito ndi manja afupikitsa kuti kusamalira.

Onani mmene mungapezere zofotokoza zapadera za malamulo khumi ku Dutoronome. Kenako tikuonetsani mmene malemba a Yohane afananira ndi malamulo athu akuthupi a masiku asanu ndawiri.

Ndondomeko yoyamba (1): Lembani Malamulo Khumi a Mulungu onse (Eks 20, Deut 5)

Malamulo Khumi a Mulungu
1. Usakhale nayo ndi milungu ina koma ine ndekha
2. Usadzipangire chofanizira chilichonse chakumwamba kapena chapadziko lapansi
3. Usagwiritse ntchito molakwika dzina la Yehova Mulungu wako



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

4. Uzisunga tsiku lasabata kuti likhale lopatulika
5. Lemekeza bambo ako ndi amayi ako
6. Usaphe
7. Usachite chigoololo
8. Usabe
9. Usaikire umboni womunamizira mzako
10. Usasilire mkazi kapena katundu wamzako

Ndondomeko yachiwiri: (2) Lembani mndandanda ogwawidwa mu tebulo

Mkagawo kotsika koyamba, lembanimo malamulo omwe ali otsutsa (monga “Zomwe Mulungu analetsa kuchita”), mkagawo kena kotsika, ikanimo malamulo omwe siotsutsa (monga “zomwe Mulungu anati tizichita”).

Zomwe Mulungu analetsa (makhalidwe oletsedwa)	Zomwe Mulungu analangiza(makhalidwe abwino)
	1. Usakhale nayo ndi milungu ina koma ine ndekha
2. Usadzipangire chofanizira chilichonse chakumwamba kapena chapadziko lapansi	
3. Usagwiritse ntchito molakwika dzina la Yehova Mulungu wako	
	4. Uzisunga tsiku lasabata kuti likhale lopatulika
	5. Lemekeza bambo ako ndi amayi ako
6. Usaphe	
7. Usachite chigoololo	
8. Usabe	
9. Usaikire umboni womunamizira mzako	
10. Usasilire mkazi kapena katundu wamzako	

Ndondomeko yachitatu (3) Muonjezere motsitsa ena malamulo achikhailidwe kumbali zonse, zoletsedwa kuziika kumbali ya Malamulo otsutsa, ndizolangiza zabwino kumbali ya malamulo olangiza.

Zomwe Mulungu analetsa (makhalidwe oletsedwa)	Zomwe Mulungu analangiza(makhalidwe abwino)
	1. Usakhale nayo ndi milungu ina koma ine ndekha
2. Usadzipangire chofanizira chilichonse chakumwamba kapena chapadziko lapansi	
3. Usagwiritse ntchito molakwika dzina la Yehova Mulungu wako	
	4. Uzisunga tsiku lasabata kuti likhale lopatulika
	5. Lemekeza bambo ako ndi amayi ako
<i>Usagalukire</i>	<i>Ukhale oleza mtima, ndi wachifundo, Aef 4:31,32</i>
6. Usaphe	<i>Ukhare ndi mtima olungama, (Jas 4:4)</i>
7. Usachite chigoololo	<i>Uzilimbikira ndi kusamala (Aef 4:28)</i>
8. Usabe	<i>Uyankhure zoona (Aef 4:25)</i>
9. Usaikire umboni womunamizira mzako	<i>Uziyamika ndi kukhutitsidwa 2 Tim 6:5,6)</i>
10. Usasilire mkazi kapena katundu wamzako	

Ndondomeko yachinayi (4): Kufupikitsa malamulo ndi zikhalibwe

Zomwe Mulungu analetsa (makhalidwe oletsedwa)	Zomwe Mulungu analangiza(makhalidwe abwino)
2. Usadzipangire chofanizira chilichonse chakumwamba kapena chapadziko lapansi (KUDZITAMANDIRA)	1. Usakhale nayo ndi milungu ina koma ine ndekha (KUDZICHEPETA)
3. Usagwiritse ntchito molakwika dzina la Yehova Mulungu wako (KUDZITAMANDIRA)	4. Uzisunga tsiku lasabata kuti likhale lopatulika (KUDZICHEPETA)




Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

<i>Usagalukire</i>	5. Lemekeza bambo ako ndi amayi ako (KUMVERA)
6. Usaphe (KUKWIYA)	<i>Ukhale oleza mtima, ndi wachifundo, Aef 4:31,32 (KUKHULULUKA)</i>
7. Usachite chigoololo (CHOYIPITSA)	<i>Ukhare ndi mtima olungama, (Yes 4:4) (CHIYEROC)</i>
8. Usabe (UMBAVA)	<i>Uzilimbikira ndi kusamala (Aef 4:28) (KUSAMALA)</i>
9. Usaikire umboni womunamizira mzako (CHINYENGO)	<i>Uyankhure zoona (Aef 4:25) (CHILUNGAMO)</i>
10. Usasilire mkazi kapena katundu wamzako (KUSILIRA)	<i>Uziyamika ndi kukhutitsidwa 2 Tim 6:5,6) (KUTHOKOZA)</i>

NDONDO MEKO ZONSE ZINAYI MWACHIDULE

Zitsutsano za Mmalamulo khumi





Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures
Ma keyala Ali mmusiwa akuonetsera kuti Miyambo, chiphunzitso Cha pa phiri, buku la Yohsne1-12, akolose3, Mariko 7:1-23, ndinso mafuko asanu ndi awiri aja deuteronomo 7:1-3, akuonetsera mndandanda wa zotsutsana mu ndime iliyonse yomwe taiona.

<http://wisdoms-house.com/G&T/V&V/VVNDtJn.html>

http://wisdoms-house.com/G&T/V&V/OldMan_vs_NewMan_vs_V&V_Col3.pdf

<http://wisdoms-house.com/G&T/V&V/7V&V.jpg>

<http://wisdoms-house.com/G&T/V&V/Visual%20V&V%20User's%20Guide.jpg>

http://wisdoms-house.com/G&T/V&V/SevenNationsHTML/HTMLFiles/Seven_Nat.html

https://wisdoms-house.com/Warfare_Against_The_Seven_Headed_Beast.pdf

https://wisdoms-house.com/Gospel_of_John_Introduction.pdf

<https://wisdoms-house.com/?p=386>

<https://wisdoms-house.com/?p=135>

1. MALAMULO KHUMI A MULUNGU NDI NSANAMIRA ZOFUNIKIRA KUMAZIGWIRITSA NTCHITO NTHAWI ZONSE

“...munthu wina anamuthamangira nagwada pa Iye nafunsa, “Ndingachite chani kuti ndilandire moyo osatha?...Ndipo Yesu anti kwa iye... Iwe umadziwa malamulo malamulo, usaphe, usachite chigololo, usabe, usapereke umboni wabodza, usachite chinyengo, lemekeza bambo ako ndi amayi ako. **Mar 10:17-19, Luk 18:1-20.**

“kotero malamulo onse awa, usachite chigololo, usaphe, usabe, usakhalire umboni wabodza, usachite chinyengo, aombedwa mkota pa lamulo ili, Konda mzako (mnansi wako) monga udzikondera iwe mwini. **Arom 13:9**

2. MALAMULO KHUMI AMULUNGU ATHA KUNENEDWANSO MWACHIDUULE KUTI NDI NTCHITO YATHU KWA MULUNGU KOMANSO NTCHITO YATHU KWA ANTHU.

“M’modzi wa aphunzitsi amalamulo anabwera... anamfunsa Iye kuti, “Mwa malamulo onse, kodi lopambana ndiye liti? Yesu anayankha kuti, Lamulo loposa onse ndi ili, Tamvani inu ana Aisraeli: Uzikonda Yehova Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi nzeru zako zonse, ndi mphamvu zako zonse ndipo lachiwiri lake nali konda mnansi wako monga iwe mwini. Palibe lamulo lakuposa awa”. **Mar 12:28-29, Luk 10:27-28, Mat 22:35-37, Deut 6:4, Arom 13:9.**

3. MALAMULO A MOSE ANAPANGIDWA KUTI ATIPUNIZITSE NSANAAMIRA ZA MALAMULO KHUMI A MULUNGU.

“...koma ine sindikadazindikira tchimo, koma mwalamulo ndimo, pakuti sindikadazindikira chilakolako, sichikadati chilamulo, usasilire. “ **Arom 7:7**

“momwemo chilamulo chinakhala namkungwi wathu wakutifikitsa kwa kwa Khristu.” **Agal 3:24**



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

**4. NSANAMIRA ZA MALAMULO KHUMI A MULUNGU
ZINAFOTOKOZEREDWA MWANDONDOMEKO MMALEMBA A
DEUTOROME KUYAMBIRA NDIME 6:4.**

Mmene malamulowa anagawidwira sizikutengera mmene ndime za bukuli zinagawidwira. Mutha kuonako mmene zinafotokozeredwa mwachidule mmusimu. Muthanso kuwerengako uku “Walter C. Kaiser Jr. “Toward Old Testament Ethics” Ndime 8.”, Lamulo La Deutoronome.

**5. PANGANO LA MOSE (MALAMULO) LITSATIRA PANGANO LA
ABRAHAMU (CHIKHULUPIIRO)
Arom 4:1-25, 2 Pet 1:5, Arom 13:9**

Kodi Mukutha Kuona Izo Zikufana Tanthauzo?

Ndondomeko Ya Kapangidwe Ka Malamulo Bukhu la Aphunzitsi

Mau a Baibulo	Chifupikitso cha chikhalidwe	Kufotok oza za uchimo (chikhali dwe)	Malamulo Khumi (Deut 5:6-21)	Kufotok oza zabwino (Chikhali dwe)	Chifupikitso cha chikhalidwe	Mau a Baibulo
			1. Usakhale nayo ndi milungu ina koma ine ndekha	X	1. Kudzichepetsa	Deut 6:4, Mar 12:29-31
Deut 7:1-26	1. Kudzitamandira	X	2. Usadzipangire chofanizira chilichonse chakumwamba kapena chapadziko lapansi			
Deut 9:6-29	Kudzitamaandira	X	3. Usagwiritse ntchito molakwika dzina la Yehova Mulungu wako			
			4. Uzisunga tsiku lasabata kuti likhale lopatulika	X	Kuddzichepetsa	Deut 8:1-9:5 Mar 2:27
Deut 9:6-29	2. Kugalukira		5. Lemekeza bamboo ako ndi amayi ako	X	Kumvera	Deut 10:1-18:22
Deut 19:1-22:8 Mat 5:21-26	3. Kukwiya	X	6. Usaphe		Kukhululuka	Deut 19:1-22:8
Deut 22:9-23:18 Mat 5:27-30	4. Choyipitsa	X	7. Usachite chigololo		Chiyero	Deut 22:9-23:18
Deut 23:19-25:12	5. Umbava	X	8. Usabe		Kulimbikira	Deut 23:15-25:12
Deut 25:13-26:9	6. Chinyengo	X	9. Usaikire umboni womunamizira mzako		Chilungamo	Deut 25:13-27:7
Mat 6:19-35	7. Kusilira	X	10. Usasilire mkazi kapena katundu wamzako		Kuyamika	Deut 27:8-30:20

Kuti mumvetsetse zili mu tebulo lili pamwambari, tsatirani izi:

1. Malamulo khumi a Mulungu ayikidwa pa mpata uli pakati (mpata wachinayi)



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

2. Zaikidwa kuti ngati lamulo likufotokoza za khalidwe labwino kapena zakhalidwe loipa (lotsutsana), chilembo cha “X” chaikidwa mkabokosi koyenera.
3. Chifupikitso cha chikhalidwe chaikidwa mu mpata wachiwiri kapena wachisanu nchimodzi ngat ndi chifupikitso cha chikhalidwe chabwino kapena choipa; mawu awa ndiongopangidwa.
4. Ndipo pomaliza, ndime za mbuku la Deutorome omwe akufotokoza za zikhalidwe zalembedwazi ayikidwa mumpata oyambilira komanso omalizira.

Dziwani kuti mawu a mBaibulo wo ayikidwa mndondomeko yake. Ndime yomwe yayikidwa mmagawo awiri a mmwambawo, Marko 7:21-23, ikukamba za zikhalidwe zomwe zaikidwa mmagawo amenewo.

Kufotokoza chikhalidwe chilichonse pachokhapachokha

KUDZICHEPETA

Kuchokera ku buku la Deutoronomo

“Ine ndine Yehova Mulungu wako amene ndinakutulutsa ku Iguputo, mdziko la ukapolo...”
Deut 5:6

“Koma kumbukirani Yehova Mulungu chifukwa ndi amene amakupatsani, mphamvu zopezera chuma...” Deut 8:18

Tanthauzo: kudzichepetsa, kumafanana ndi kufatsa, kumabwera ukazindikira zomwe Mulungu amatichitira kudzera mwa chikondi chake.

Zoyenera kudziwa

Kumulambira Mulungu ndi kukumbukira zomwe Mulungu amatichitira mmoyo mwathu ndi mmene timapewera kudzikweza (kunyada). Kumulambira Mulungu ndilo lamulo loyamba.

Kukumbukira dzanja la Mulungu pazochita zathu ndi lamulo lathu lachinayi.

Zitsanzo za m’Baibulo: Luka 18:9-14
Davite, Masalimo 139,51,32
Mose, Numeri 11:24-30, 12:3, Masalimo 90
Davite Vs Goliati 1 Sam 17:37
Luka 14:8-11, Miyambo 27:2
Kudzichepetsa ngati mwana, Mateyu 18:1-7

KUDZITUKUMULA (KUDZITAMANDIRA)

Kuchokera ku buku la Deutoronomo

“Usadzipangire chofanizira chinthu chilichonse ... usatchule dzina la Mulungu pachabe...” Deut 5:8

Deut 8:11-17 ikutionentsa mmene timafikira ku kudzitama, “salamani kuopa kuti mungayiwale Yehova Mulungu wanu posasunga malamulo, zikhazikiko ndi malangizo ake amene ndikupatsani lero, kuopa kuti mukadya ndi kukhuta, mukamanga nyumba zabwino ndikukhalamo... **mtima wanu udzayamba kunyada ndikumuyiwala Yehova Mulungu wanu...** muntima mwanu mukhozakuganiza kuti, mphamvu zanga ndi kulimbikira kwa dzanja langa ndizimene zandilemeletsa chonchi...”

Tanthauzo: Maganizo akudzikweza, makani, kudzitamandira, kapena kutamandira zinthu zina, kudzitukumula, kumadza Kamba kokanika kuona dzanja la Mulungu pa moyo wa munthu, kuyamikiridwa pa ntchito yoti ndi ya Mulungu.

Zoyenera kudziwa

Munthu amalambira Mulungu, zinthu zapadziko kapena iye mwini. Kulambira zinthu ndiko kulambira mafano, kudzilambira ndiko kudzitamandira. Kulambira mafano komanso kudzitamandira kulli ndi tanthauzo limodzi.

Aroma 1:21 ikutionentsa mmene kulambira mafano kumakhalira: “...ngakhale iwo amamdziwa Mulungu, sanamulemmekeza ngati Mulungu, ...ndipo anasanduka wachabechabe mmaganizo awo, ndipo mmitima yawo munadzadza mdima. Ngakhale ankadzitama kuti ndi anzeru



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

(kudzitamandira), anasanduka opusa. Iwo anasinthanitsa ulemerero wa Mulungu wosafa ndi mafano opangidwa ndi manja wooneka ngati munthu... (kupembedza mafano ndi kudzitamandira)".

Masalimo 10:3 akutionetsa mmene kudzitukumula kumatsutsira Mulungu: “iye amatamandira zokhumba mumtima mwake, amachitira chipongwe Yehova, Mulungu Sali mmalingaliro ake onse”. Kuchotsa Mulungu mmoyo mwathu ndiko kudzipanga osakhulupilira. Kuika Mulungu mmoyo mwathu ndiye kudzipatula kapena kukhala opatulidwa.

Chitsiru chimati mumtima mwake kullibe Mulungu (Sal 14:1). Uchitsiru ndi kudzitamandira izo nzofanana mmatanthauzo.

Zitsanzo za m’Baibulo: Afarisi, Luka 18-9-14/ Nebugadinezala, Daniele 4:29-37
Sauli, 1 Samuele 15
Mafano a munthu, Yesaya 44/ Fano lili ngat olipanga, Sal 135:15-18
Masa ku Deuteronomo akukumbuukira Eks 17:7 mmene ana a Israeli
Anayesa Mulungu kunena kuti, kodi Mulungu yo ali ndife kapena ayi
Mkhuto umayambitsa kudzitamandira Miyambo 30:8,9,22]

KUMVERA

Kuchokera ku buku la Deuteronomo

Lemekeza bambo ako ndi amayi ako, monga Yehova Mulungu wako wakulamulira iwe, kuti ukhale ndi moyo wautalli, ndikuti zikuyendera bwino mdziko limene Yehova Mulungu wako akukupatsa... Deut 5:16

“sungani mawu anu mumtima mwanu ndi mmaganizo mwanu... mawuwa muziphunnzitsa ana anu, muzikamba za iwo pamene mukhala pansu mnyumba zanu, pamene mukuyenda mnjira, pamene mugona ndi pamene mukudzuka”. Deut 11:18-19. “mukatsatira mosamalitsa malamuwu omwe ndikupatsaniwa, ndikuwachita...” Deut 11:22

Tanthauzo: Kumvera atsogoleri; kudzikhuthura komanso kutsatira ndondomeko.

Kumvera atumiki a Mulungu

Makolo ndi otiyang’anira (Deut 11)

Malamulo a mmadela (Deut 12:1-16-17, Jas 2:14:18, 1 Yoh 4:19-21)

Mafumu (Mafumu)

Malamulo a boma (Deut 16:18-22, 17:2-7)

Malamulo a chitaganya (Deut 17:8-13)

Mfumu (Deut 17:14-20)

Abusa (Deut 18:1-14)

Alosi, ndi alangizi (Deut 18:15-22)

Zitsanzo za m’Baibulo: Khutu la Samuyeli omvera Sam 3

Abulahamu apereka mwana wake Kamba kakumvera Gen 22:1-19

Yesu anamvera za imfa Yake Fil 2:8

Kumvera kwenikweni kumaoneka muzochita, osati mawu Mat 21:28-31

Kunyumba ya munthu owumba mbiya Yer 18:1-23

Ulamuliro wa makolo Aef 6:1-4

KUGALUKIRA: Kuuwukira zonena za ena, Deut 5:16

Kuchokera ku buku la Deuteronomo

“...kumbukiran izi ndipo musayiwale mmene munaputula mkwiyo wa Yehova mchipululu muja. Kuyambira tsikuk limene munatuluka mu Iguputo mpaka pamene munafika kuno, mwakhala owukira Yehova”. Deut 9:7-8. “kotero chitani mdulidwe wa mmitima yanu ndipo musakhalenso opulupudza.” Deut 10:16.



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

Tanthauzo: Kukana kulumulidwa (kuwukira), kukana kumvera, kukhala waliuma, kukhala wopulupudza kapena kuchita zofuna zawo.

Zitsanzo za m’Baibulo: Kuwukira kwa ana a Eli kuphwasulidwa 1 Sam 2:22-36
Sauli, “Kuwukira kuli ngati tchimo la umfiti”, 1 Sam 15
Kola awukira Mose ndi Aroni, Num. 16, Matt 23:2
Israyeli ogalukira afuna mfumu, 1 Sam 3
Ayuda akana kumvera Sitifano, Mach 8:51-57
Mtsuko owumba osalimba, Yer 19:1-15
Chitsime chophwera, Yer 2:13

KUKHULULUKA: Mau otsutsana ndi “usaphe”, Deut 5:17

Kuchokera mu buku la Deutoronome

“akulu...adzasamba manja awo ndi mwazi wa nkunzi yomwe yadulidwa mutu...Tichitireni chifundo, Oh Ambuye...deut 20:6-8)

Tanthauzo: Kusiya kukhala ndi mangawa kwa ena, kukhala ndi chifundo ndi ena, kumasula a ngongole kapena okulakwira, kuwaphimba kapenanso kuwathandiza.

Kuchitira chifundo okaikilidwa (Deut 19:1-10)
(mizinda ya mpumulo)

Chifundo chopatsidwa (Deut 19:14)

Chifundo kwa antchito asanayambe ntchito zawo (Deut 20:5)

Chifundo kwa mwini malo watsopano (Deut 20:6)

Chifundo kwa akwati atsopano (Deut 20:7)

Chifundo kwa iwo otayamtima (Deut 20:8,9)

Chifundo kwa adani (Deut 20:10-15)

Chifundo kwa zinthu za mnthaka (Deut 20:19-20)

Chifundo kwa osachimwa (Deut 21:1-9)

Chifundo kwa ogwidwa kunkhondo (Deut 21:10-14)

Chifundo kwa oyamba kubadwa (20:15-17)

Chifundo kwa otembereredwa (oyipa) (Deut 21:22-23)

Chitirani chifundo zinthu zamzanu (Deut 22:1-4)

Chitirani chifundo zolendedwa zamtchire (Deut 22:6-77)

Chitirani chifundo awo osakaikiridwa, ofooka, opanda zodzitetzera, olakwitsa (Deut 22:8)

Chitirani chifundo awo anapha anzawo mosalingalira (Deut 19:10-13, 1 Akor 5:1-5)

Chifundo za mboni ziwiri (Deut 19:15-21)

Kuti tisabweze choipa komanso kukhetsa mwazi

Chifundo cha nkondo ya Mulungu (Deut 20:1-4, 1 Akor 5:1-5)

Chifundo ku thupi la anthu aku Kanani (Deut 20:16-18, 1 Akor 5:1-5)

Chitirani chifundo mwana owukira (Deut 21:18-21, 1 Akor 5:1-5)

Chifundo kwa ophwanya lamulo la Mulungu (deut 22:5, 1 Akor 5:1-5)

Zitsanzo za m’Baibulo: Yosefe akhululukira abale ake, Gen 50:7

Mulungu akhululuka kugwiritsa ntchito njoka mtengo, Num 23, Yoh 3:14

Yesu pamtanda, Luka 23:24

Abigelo athandiza Davite kukhululuka, 1 Sam 25

Mfunu yokhululuka Mat 18:21-35)

KUWAWIDWA MTIMA: “Usaphe” Deut 5:17

Kuchokera m’buku la Deutoronome

“Koma ngati wina mwa inu amuda m zake namubisalira panjira namuvulaza mpaka kumupha...musamumvere chisoni...” Deut 19:10-13.



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

Tanthauzo: Kupha, Mat 5:21-26. Kusunga ngawa, kukhala ndi mtima ofuna kuvulaza wina, kukhala ndi chidani kapena malingaliro aupandu kwa wina, kubaya, kupanda chikondi, kukhala owawa.

Zitsanzo za m’Baibulo: Kuwawidwa mtima ndi kupha, Mat 5:21-26
Kaini ndi Abele, Gen 4:1-9
Aisrayeli akwiyira Mose ndi Mulungu, Num 21:4-9
Davite awawidwa mtima ndi Nabala 1 Sam 25
Kaini apha Abele, Gen 4
Jezebelo alondalonda Eliya, 1 Maf 19
Mtumiki wosakhululuka, Mat 18:21-35
Kuwawidwa mtima ndi uchimo, 1 Yoh 2:8-11, Yak 3:8-18

KUYERA MTIMA (kupatulika): Mau otsutsana ndi “kupha”

Kuchokera m’buku la Deutoronome

“...pakuti Yehova Mulungu wanu amayendayenda ku msasa wanu kukutchinjilizani ndikupereka adani anu kwa inu. Nchifukwa chake msasa wanu uzikhala opatulika kuti mwina angaone china chonyansa nabwelera osakuyandikirani. Deut 23:14

Tanthauzo: kukhala osasunthika, osasokonezeka, kukhala mchiyero, osonongeka kapena kuipitsidwa, kupanga zoyenera kupanga,...

Kudzipatula ku ena osaenera (Deut 22:10)
Kudzipatula ku odziononga okha (Deut 23:1)
Kudzipatula ku osakhulupilira (Deut 23:2-6)
Kumacheza ndi okhulupilira (Deut 23:7,8)
Kudzipatula ku umve
Ukhondo munthu (Deut 23:9-11)
Nyansi ndi zinyalala Deut 23:12-14)
Kucheza ndi othawa maiko ena osowa thandizo
Kudzipatula kwa ochimwa osalapa
Okwatirana okhaokha, monga aku Sodomu (Deut 23:17)
Ochita zachimasomaso (uhule) (Deut 23:17,18)

Zitsanzo za m’Baibulo : Kudzichotsa manyazi (Mat 5:29,30)
Shadileki, Misheki ndi Abedenigo akana kulambira fano, Dan 3
Yosefe apewa mkazi wa Potifala, Gen 39
Chodetsedwa tidane nacho Aef 5:1-14.

CHOIPITSA: “Usachite chigololo” Deut 5:18

“musadzale mbewu zamitundu yosiyana mmmunda wanu wa mpesa, ngati mutero, si mbewu zanu zokha zimene zidzakhale zodetsedwa komanso zipatso za mmunda wa mpesawo.

Tanthauzo: kuchidetsa, kuchisakaniza, kunyenga, kupotoza kapenga kunyengeza, kunyasitsa poonjezera zinthu zina zoipa, kuwonjezera zina zachilendo, kusachita chinthu cholondola.

Kuipitsa munda wa mpesa (Deut 22:9)
Kuipitsa zopangira zovala (Deut 22:11,12)
Kuipitsa mwa mkwatibwi (Deut 22:14-21)
Kudetsedwa mchigololo (Deut 22:22-24)
Kudetsedwa mu kugwilirira (Deut 22:25-27)
Kudetsedwa mkuchita chiwerewere (22:28-29)
Kudetsedwa mkukwatirana pachibale, mchisokonezo, zinthu zolawula (Deut

22:30)

Zitsanzo za m’Baibulo: Chilakolako ndi chigololo (Mat 5:27-28)
Chiyambi cha Samisoni, Maf 14:1-3, Deut 7:1-4
Samisoni ndi Delila, Mapeto, maf 16
Davite ndi Betiseba, 2 Sam 11
Solomo aipitsa Israeli ndi akazi, 1 Maf 11:1,2



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

Rebobowamu aipitsa Aisraeli ndi uphungu oipa 1 Maf 12:18
Maganizo amadetsa ngat zochita, Mat 5:27-30, Mal 7:21-23

KULIMBIKIRA

Kuchokera mu buku la Deutoronome

“mukalumbira kupereka kanthu kwa Yehova Mulungu wanu, musamachedwetse kupereka, chifukwa Yehova Mulungu wanu adzakufunsanibe kanthuko ndipo mudzapezeka kuti mwachimwa, ...muzikwanilitsa...zilizonse zomwe mulumbira ndipakamwa panu, muzitsimikiza pakuzichita ...” Deut 23:21-23

Tanthauzo: Kukwanilitsa udindo, ntchito, kapena zochita, kupililira, khama ndiponso kumalizitsa. Ndi ndondomeko yopanga chilichonse chotheka kuti umalize ntchito, kugawa zinthu zogwilira ntchito moyenera.

Zoyenera kudziwa:

Kulimbikira kumayambira mu kudzipereka, kudziwa udindo, kudzikhuthura kapena kulimbira. Kukhala olimbikira, munthu ayenera, kusiya kapena kuyenera kapena kukhazikika pa ntchito imodzi, cholinga kapena chifukwa chimodzi.

Kulimbikira polumbira (Deut 23:21-23)

Kulimbikira mukuchita zachifundo ndi udindo (Deut

Kulimbikira poika zina patsogolo maudindo ena (Deut 24:5)

Panyumba, kumpingo ndi mbali zina za dziko

Kusamalitsa pomvera ndikuchita chilungamo (24:8,9)

Kusamalitsa pa maufulu a ovutika (Deut 24:10-13)

Kusamalitsa pachilungamo (Deut 24:16-18)

Kusamalitsa pamafuno anu, zachifundo, ndi kusakondera (Deut 24:19-22)

Kulimbikira posamalira banja (Deut 25:1-3)

Kusamalitsa chilungamo: kuthandiza komanso kulimbikitsa ena (Deut 25:11-12)

Zitsanzo za m’Baibulo: Kuchenjeza kulumbiliratu, guwa, malonjezano Mat 5:33-37

Malipiro a Mulungu Sali mmoyo uno Mat 5:33-48

Nowa anapilira posatengera zovuta za osakhulupilira, Gen 6, Aheb

11:7

Phunziro la kudzipereka kwa nyerere Miy 6:6-11

Miy 10:4, 27:23-27, Aef 4:28

Kulimbikira mu uzimu: Yoh 6:26-27

Kukondera, kuweruza ndi chifundo: Jas 2:1-13

UMBAVA: “Usabe”, Deut 5:19

Kuchokera m’buku la Deutoronome

“Ngati munthu agwidwa akuba...wakubayo akuyenera kufa...” Deut 24:7

Tanthauzo: Kutenga chinthu chomwe chili cha munthu wina, kusokoneza nthawi, ndalama kapena zinthu; kunyalanyaza ntchito, kukhala waulesi kapena kukana kugwira ntchito, kuba zing’onozing’ono, kukopa.

Zoyenera kudziwa:

Umbava umayamba ukalephera kudzipereka, kusiya, kapena kulongosola zinthu pa ntchito kapena zina. (Deut 24:7, 25:4)

Umbava popanga katapila (Deut 23:19-20)

Umbava popanga zisudzulo (Deut 24:1-4)

Umbava potenga zikole (Deut 24:6)

Umbava pa kuba (Deut 24:7)

Umbava popondereza (Deut 24:14-15)

Umbava posalipira antchito moyenera/ zipepeso (Deut 25:15)

Zitsanzo za m’Baibulo: Akan abela adani, Yos 7

Davite aba nkazi, 2 Sam 11

Yakobo aba ukulu wa m’bale wake, Gen 25



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

Njira ulesi za munthu Miyambo 24:30-34

CHILUNGAMO: mawu otsana ndi kunama, kukhalira umboni wabodza, Deut 5:20

Kuchokera m’buku la Deutoronome

“muyenera kukhala ndi miyeso ndi milingo yoyenera nd yosanyenga...” Deut 25:15

Tanthauzo: Kukhala weni weni, wosanama, wachilungamo, oyenda mowongoka.

Zitsanzo za m’Baibulo:

Yeremiya achenjeza Aisrayeli, Yer 1:6-10

Eliya achenjeza Ahabu ndi Jazibelo, 1 Maf 17, 18

Natani ayankhula kwa Davite 2 Sam 12:1

Samuelli ayankhula kwa Eli, 1 Sam 3

CHINYENGO:

Kuchokera m’buku la deutoronome

“Usaperekere umboni wabodza wa mzako” Deut 5:20

“Sindinapatuke pazimene munalamula kapena kuyiwala ndi chimodzi chimwe...” Deut 26:13

Tanthauzo: Kkukhala wabodza, zochita zonama, kusokeretsa ena, kukhala ndi khalidwe

lokwawa ngat nyama za mgulu la njoka. (Gen 3:14)

Kunyenga ponena zabodza (Deut 25:13-16)

Chinyengo cha Aamelaki (Deut 25:17-19)

Zitsanzo za m’Baibulo:

Chiphamaso: (Mat 6:1-18)

Pa sadaka (Mat 6:1-4)

Popemphera (mat 6:5-15)

Posala (Mat 6:16-18)

Yakobo adanyenga Isake, Gen 27

Akani abisa zakuba, 1 Maf 21

Gibiyoni apusitsa Yoswa, Yos 9

Hananiya ndi Safira adzinyenga okha, Mach 5

KUTHOKOZA: mawu otsutsana ndi mtima osilira, Deut 5:21

Kuchokera m’buku la Deutoronome

Tanthauzo: kukhutitsidwa, kuyamika kapena kusangalala chifukwa cha zomwe Mulungu wakupatsa.

Deut 26:11. “Ndipo inu ndi Alevi pamodzi ndi alendo obwera mudzakondwera mzinthu zonse zabwino zimene Yehova Mulungu wanu wakupatsani inu ndi apabanja panu.”

Kuyamika pokumbukira zomwe Mulungu watipatsa (Deut 26:1-11)

Kuyamika pakupereka chakhumi (Deut 26:12-15)

Kuyamika pakuikirapo mtima (Deut 26:16-19)

Kuyamika poika miyala yachikumbutso (Deut 27:1-8)

Zitsanzo za m’Baibulo:

Zomwe Mulungu amatipatsa tsiku lililonse (Mat

6:25-35)

Ana ndi Elikana apereka Samueli kwa Mulungu 1 Sam 1

Yobu atamanda Mulungu pazomwe zataika, Yobu 1

KUSILIRA:

Kuchokera m’buku la Deutoronome

“Usasilire mkazi,...nyumba,...munda..” Deut 5:21

Tanthauzo: kusakhutitsidwa ndizimene alinazo, kukhala ndichilakolako chosayenera pazinthu zimene alibe, kumapangitsa kukhulupilira mu chuma chapadziko ndi kukonda zapadziko. (1 Yoh 2:15-17)

Zitsanzo za m’Baibulo:

Kusunga chuma chachinyengo (Mat 6:19-20)

Chuma chako ndiye mulungu wako (Mat 6:21)

Chophimba chaa kupembedza mafano (Mat 6:22-24, Akor

3:5b)



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

Ahabu asilira munda wa mpesa wa Naboti, 1 Maf 21

Gehazi asilira katundu wa Asiriya, 2 Maf 6:20-27

Akani asilira katundu wa adani, Yos 7

Chikondi cha ndalama, 1 Tim 6:5-10

Samalani ndi kusilira, Luk 12:13-21

ZIKHALIDWE ZOIPA NDI ZAB WINO MMAWU ABWINO A YOHANE (kuyambira zakumunsi)

Kusilira: Yoh 11:48, ikutionetsa kuti Yesu anaphedwa chifukwa cha kusilira(nsanje). “Ngati ife timuleka kuti apitilize chotere, aliyense adzamukhulupilira Iye, ndipo kena Aroma adzabwera ndikudzatenga malo athu pamodzi ndi dziko lathu”

Kuyamika: Yoh 11:41-46, Ikutionetsa kuthokoza kwa Yesu kwa Atate, “Iye anayang’ana kumwamba nati, “Atate ine ndikuthokoza chifukwa mumandimvera. Ine ndimadiwa kuti Inu mumandimvera nthawi zonse. Yesu atanena izi, anakuwa kuti “Lazaro tluluka!” ndipo Lazalo anatuluka” Ndime iyi ikutionetseratu chiyamiko pakuukanso. “Ssangalalani ndi kukhla ndichimwemwe popeza mphoto yanu ili kumwamba.” **Mat 6:12.**

Chinyengo

Chinyengo ponamiza

Yoh 6:70, “Kodi ine sindinakupatsani inu khumi ndi awiri? Komabe mmodzi wa inu ndi mdiererekezi”

Yoh 7:22, “Koma, chifukwa chakuti Mose anakupatsani malamulo, komabe palibe wina mwa inu amene asunga lamulo? Mchifukwa chani mukundipsera mtima ine?”

Yoh 8:40-44, “Koma mmene zililimu, inu mwatsimikiza kundipha Ine, munthu amene ndakuuzani chhonadi...inu ndinu ana amdyerekezi ndipo inu mukufuna kuchita zimene abambo anuwo akukhumba. Iye anali wakupha kuyambira pachiyambi, sanasunge choonadi, pakuti wa iye mulibe chhonadi. Pamene iye anen bodza, amayankhula chiyankhulo chobadwa nacho popeza ndiwabodza ndipo ndi bamboo wamabodza...”

Kudzinyenga: “mukanakhala osaona, simukanachimwa: koma tsopano popeza mukuti mumona, chonchondinu ochimwabe.” **Yoh 9:1-41**

Chilungamo (kunena zoona)

Yesu aonetsa chilungamo cha Atate, **Yoh 7:28**, “koma iye amene anandituma ine ndi woona...”

Yesu aonetsa chilungamo chenicheni mwa ife. “uyo adziwa kuti sanachimwepo, aponye mwala oyamba...” **Yoh 8:7**

Yesu aonetsa chilungamo pa maumboni ake mu **Yoh 8:14-18**, “Ngakhale ndidzichitira umboni umboni wangawu ndi woona... ine ndikati ndiweruze, ndimaweruzza molondola...zinalembedwa



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures
mmalamulo anu kuti umboni wa awiri ndiwovomerezeka...Ine ndikudzichitira umboni ndipo
mboni inanso ndi Atate amene anandituma...”

“...ndipo choonadicho chidzakumasulani...” **Yoh 8:32**

Otsatira Abulahamu mchoonadi: **Yoh 8:40-47**

Kusiyana kwa wakuba ndi m’busa wa nkhusa: **Yoh 10:1-19**

Kusiyana kwa mwini wa nkhusa ndi m’busa wankhusa: **Yoh 10:11-18**

Kuba: Zochita za opanda chikhulupiliro

Nduna ya mfumu Yohane 4:46-54

Munthu olumala Yohane 5:1-14

Kugwira ntchito **Yohane 6:27-58**: “Gwiran ntchito, osati chifukwa cha chakudya chimene
chimawonongeka koma chifukwa cha chakudya chimene sichiwonongeka mpaka kun koyo
wosatha...”

Kulimbikira: ntchito za okhulupirika

Ntchito ya mwana “Chakudya change ndikuchita chifuniro cha iye amene anandituma
ndikumaliza ntchito yake”

Zokolora: **Yohane 4:34-38**

Zaokolora za okhulupirika: ngakhale tsopano amene akukolora akulandira malipiro ake, ndipo
akututa mbewu ku moyo wosatha...” **Yohane 4:36**

Mwana alimbikitsa okhulupilira 5:21

Zomwe okhulupilira amapeza 6:1-12

Kusamala kwa okhulupilira 6:12 “...tolani zotsala kuti pasawonongeke kanthu”

Kugwira ntchito za muyaya Yohane 6:27

Mkate wa moyo Yohane 6:32-58

Choipitsa:

“Kuwunika kunabwer padziko lapansi, koma anthu anakonda mdima mmmalo mwa kuwunikako
chifukwa ntchito zawo zinali zoyipa. Aliyense ochita zoyipa amadana ndi kuunika ndipo
sabwera poyera chifukwa cha mantha kuti ntchito zake zingaonekere.” Yohane 3:19.

Mzimayi wa ku Samariya pachitsime: Popeza Ayuda ndi Asamariy sankayanjana: Yohane 4:9,
Deut 7:1-5

Kooma zoonza nzakuti wakhala pabanja ndi amuna asanu, ndipo mamuna amene uli naye pano
siwako. Yohane 4:18.



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

Ndipo tsopano ophhunziira ake anabwera namupeza akuyankhula ndi mmayi uja koma palibe amene anamufunsa kuti “kodi mukufuna chiyani kapena, Nchifukwa chiyani mukuyankhula naye?” Yohane 4:27

Kulungama

“Koma aliyense wakhala mu choonadi amabwera nku kuunika, kuti zionekere poyera zimene iye wachita zachitika kudzera mwa Mulungu” Yohane 3:21

“Ophunzira a Yohane anabwera kwa iye namfunsa zokhudza kukhala olungama...” Yohane 3:26.

Kuwawidwa mtima/kupha

Gwetsani nyumb ya Mulungu iyi ndipo ine ndidzayimanga mmasiku atatu. Yohane 2:19.

Kukhululuka/chifundo

Ngati momwe Mose anaikwezera njoka yamkuwa ija, chimodzimodzi, Mwana wa Munthu ayeners kukwezedwa; kuti aliyense akukhulupilira mwa iye asatayike koma akakhale nawo moyo wosatha. Yohane 3:14, Numeri 21:4-9

Pakuti Mulungu sanatume Mwana wake padziko lapansi kuti adzaweruze ayi, koma kuti akapulumutse dziko lapansi. Yohane 3:17

Kugalukira/kusamvera

Kusamveera kwa ana mu mpingo: “ndipo iye anaowa mnyumba ya Mulungu nayamba kutulutsa kunja amaene amachita malonda.

Kumvera

Khristu kwa amayi ake Yohane 2:7

Atumiki kwa Khristu Yohane 2:5,7

Khristu kwa Atate Ake Yohane 2:19, Fil 2:5-9

Kudzikweza

“...Iye anali yani?” Yohane 1:19, 22

“...Kodi iwe ukuti chani za iwe mwini?” Yonahe 1:22

Kudzichepeza

“Taonani mwana wa Nkhosa wa Mulungu!”...John 1:29,36



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

Malamulo Khumi a paphiri.

PEMPHERO LA PA PHIRI MUTU	“Musaganize kuti ndinadza kudzathetsa malamulo, koma kukwanilita” Mateyu 5:17b	
KUCHOKA KU MALAMULO KHUMI	MUTU WA PEMPHERO	LAMULO KU DEUTORONOME
6. Usaphe	Kuda munthu ndikupha Mat 5:21-26	Deut 19:1-22:8
7. Usachite chigololo	Chilakolako ndi kuchita chilakolako Mat 5:27,28 Kuchita manyazi (Mat 5:29,30)	Deut 22:9-23:18
8. Usabe	Nsudzulo (Mat 5:31-32) Kulumbiliratu, gome, malonjezano (Mat 5:33-37) Chilungamo (Mat 5:38-48)	Deut 23:19-25:12
9. Usanene bodza	Chiphamaso Pa sadaka (Mat 6:1-4) Popemphera (Mat 6:1-4) Pakusala (Mat 6:16-18)	Deut 25:13-26:9



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

10. Usasilire	Kusunga chuma cha chinyengo (Mat 6:19-20) Chuma chanu ndiye mulungu wanu. (Mat 6:21) Chidima cha kulambira mafano (Mat 6:22-24, Akor 3:5b) Zomwe Mulungu amatipatsa tsiku ndi tsiku (Mat 6:25-35)	Deut 26:10-15
---------------	--	---------------